

STRICTLY CONFIDENTIAL

2025 CWED MOCK

CHICHEWA PAPER TWO: MARKING SCHEME

GAWO A: MALAMULO A CHIYANKHULO (MALIKISI 40)

1. a. Bwera kuno. (malikisi 2)
b. Ife tikulemba mayeso. (malikisi 2)
c. Afotokoza akafunsidwa. (malikisi 2)
d. i. Kusonyeza phatikizo la madzera m'phuno e.g. ng'ombe
Kusonyeza kuti limbo 'u' losonyeza m'kati lachotsedwa. e.g. m'nyumba
Kusonyeza kuti zilembo zina zachotsedwa kuti mawu alembedwe mwachidule.
e.g. N'chiyani? (mayankho awiri okha)
ii. Kusonyeza mapeto a funso.e.g. Kodi mubwera?
2. a. i. Iye wabwera pa njinga.
ii. Nyumba yawo yayang'ana ku mpoto.
iii. mZione akudya ndi amayi ake.
b. i. Atwabi ankabwera kwathu.
ii. Adzakhala atabwera tikamadzadya.
3. a. i. Pophatikiza mphatikiram'mbuyo wonena za chimodzi ku mphatikiram'mbuyo wonena za zambiri. e.g. munthu = anthu = mu-,wa-,a-
ii. Poyang'anira agwirizanitsi e.g. Dzira lija lasweka. Li-, Ma-
b. i. Kukhala mwininkhani/mchitantchito e.g. Iwe ukuvina.
ii. Kuitanira e.g. Iwe, khala pansu.
iii. Kukhala mtsiriza tanthauzo la mnene e.g. Amene anasowa ndi iwe.
iv. Kukhala pamtherankhani wopanda chindunji e.g. Amayi aphikira iwe phala.
v. Kukhala pamtherankhani wachindunji e.g. Aphunzitsi asankha iwe.
vi. Kukhala mwini chinthu e.g. Ichi ndi cholemba cha iwe.
(Mayankho atatu okha)
4. a. i. Akumata
ii. matidwa
iii. matika
b. i. Pophatikiza dzina 'mwana' ku dzina lina 'mphepo' ndikupanga dzina.
ii. Pophatikiza mphatikiram'mbuyo 'm' ku tsinde la mnene 'tula' ndi kusintha limbo la mtsekulanjira 'a' wa kumapeto kwa mnene 'tula' kukhala 'o'.
c. Tumani ndi mtsikana waulemu.
d. Aphunzitsi anauza ophunzira kuti asamalongolole m'kalasi.

GAWO B: KUMVETSA NKHANI NDI KUSANTHULA CHIYANKHULO (MALIKISI 20)

- a. Zakudyazi ndi mgodo. (malikisi 1)
- b. Pamene kwachitika maliro. (malikisi 2)
- c. Atha kuwaitana kuti akalembetse zolandira chimanga, fetereza ndi zina. (malikisi 1)
- d. Anapita mwa unyinji ataitanidwa ndi mfumu. (malikisi 2)
- e. i. Amayi azipita ku sikelo akakhala oyembekezera. (malikisi 1)
ii. Atsikana asamatenge mimba ali achichepere. (malikisi 1)
(Yankho limodzi lokha)
- f. i. Ntchito zimasowa chifukwa cha kuchulukana. (malikisi 1)
ii. Malo olima amasowa chifukwa cha kuchulukana. (malikisi 1)
iii. Zachilengedwe zitaonongeka chifukwa cha kuchulukana. (malikisi 1)
(Mayankho awiri okha)
- g. i. Kuvala kondomu. (malikisi 1)
ii. Kutseketeratu kwa moyo wonse. (malikisi 1)
- h. Amathanso kudziteteza kutenga matenda opatsirana kudzera nkugonana. (1)
- i. i. Ana amakula mwathanzi. (malikisi 1)
ii. Amayi atha kukhala ndi matupi amphamvu. (malikisi 1)
iii. Makolo amatha kulera ndi kusamalira ana mosavuta, (malikisi 1)
(mayankho awiri okha)
- j. i. Akugona (malikisi 1)
ii. mwaulere (malikisi 1)
iii. aena amwalira (malikisi 1)
- k. i. Makedzana (malikisi 1)
ii. Kufuya (malikisi 1)

GAWO C: CHIMASULIRO (MALIKISI 15)

ZACHILENGEDWE

Zachilengedwe zikutha mwa njira yodetsa nkhwana m'dziko mwathu muno./Pali mantha wasapeweka kuti mosakhalitsa/mitundu yofunikira ya zomera ndi nyama itha kuzimirira./Moti ana obwera mtsogolo sadzatha kukhala ndi mwayi woona zambiri mwa izo./

Chimenenso chili chopweteka koposa/ndi chakuti chitukuko cha dziko/chimadalira kwambiri pa zolengedwazi./Zoonza zake ndi zakuti zimene timazitchula kuti luso makono/sichina kupatula kusanduliza kwa zachilengedwe/kukhala zinthu zimene ndi zokonzeka kugwiritsidwa ntchito./

Izi zikutanthauza/ kuti ngati tikufuna kufikira chitukuko cholozeke ngati dziko,/chinthu chimodzi chofunika chimene chiyenera kuchitika/ ndicho kubwezeretsa zachilengedwe zobwezeretseka,/

(Gawo lililonse malikisi 1. Mutu malikisi 1 chifukwa pagwiridwa ntchito youmasulira.)

GAWO D: CHIFUPIKITSO (MALIKISI 15)

Kusintha kwa nyengo/kwakhudza dziko lonse lapansi./

Kusintha kwa nyengoku/ kumadza chifukwa cha/kuonongeka kwa chilengedwe/mpweya woipa/wam'makampani ndi m'mafakitole/ndi mankhwala osiyanasiyana ambewu,/

Kusintha kwa nyengoku/ kumabweretsa chilala,/kusefukira kwa madzi,/matenda apakhungu/ ndi kutha kwa mitundu ya zomera ndi nyama./

(Gawo lililonse lilil ndi malikisi 1, kupatula mutu ulibe malikisi chifukwa wangotengedwa kuchokera ku nkhani.)